

Kuyenda Ndi Mulungu

CHICHEWA

Written by Rev. Lindsay Cameron.

Based on 6 studies by Rev. Paul Meeks -
“God, You and New Life”

Translated by Alexander M. Mbewe.

Published by:

The Wesleyan church
P.O.3457, Dalview 1544, Rep. Of South Africa.

International Headquarters:
6060Castleway West Drive, Indianapolis Indiana, USA
P.O.Box 50434, Indianapolis IN 46250-0434, USA.

(C) 2003 The Wesleyan Church
For permission to reprint any part of these studies,
contact the publisher.

Kodi ndinga tsimikize kuti ndine Mwana wa Mulungu?



Kuyenda ndi Mulungu
1

1 John 5: *[9]Ngati tilandira umboni wa anthu umboni, wa Mulungu uposa; chifukwa umboni wa Mulungu ndi uwu, kuti anachita umboni Mwana wache.[10]Iye amene amkhulupirira Mwana wa Mulungu ali nao umboni mwa iye ; iye wosakhulupira Mulungu anamuyesa Iye wonama; chifukwa sanakhulupirira umboni wa Mulungu wa Mulungu amuchita wa Mwana wache. [11]Ndipo uwu ndi umboni wo, kuti Mulungu anatipatsa ife moyo wosatha, ndipo moyo umene uli mwa Mwana wache. [12]Iye makhukhala ndi Mwana ali nao moyo; wosakhala ndi Mwana wa Mulungu alibe moyo.*

[13]Izi ndakulemberani kuti mudziwe kuti muli ndi moyo wosatha, inu amene mukhulupirira dzina la mwana wa Mulungu. [14]Ndipo uku ndi kulimbika mtima kumene tiri nako kwa Iye, kuti ngati tipempha kanthu monga mwa wa chifuniro chache, atimvera; [15]ndipo ngati tidziwa kuti atimvera chiri chonse tichipempha , tidziwa kuti tiri nazo izi tazipempha kwa Iye. [16]Wina akaona mbale wache alikuchima chimo losati la kuimfa, apemphere Mulungu, ndipo Iye adzapatsiramoyo wa iwo akuchita machimo osati a kuimfa. Pali chimo la kuimfa: za ililo sindinena kuti mupemphhere. [17]Chosalungama chiri chonse chiri uchimo; ndipo pali chimo losati la kuimfa. [18]Tidziwa kuti yense wobadwa kuchokera mwa Mulungu sachimwa,koma iye wobadwa kuchokera mwa Mulungu adzisungayekha , ndipo woipayo samkhudza. [19]Tidziwa kuti tiri ife ochokera mwa Mulungu , ndipo dziko lonse lapansi ligona mwa woipayo. [20]ndipo tidiwa kuti Mwana wa Mulungu wafika, natipatsa ife chidziditso, kuti tizindikire Woonayo, mwa Mwana wache Yesu Khristu . Iye ndiye Mulungu woona ndi moyo wosatha.

Lowezani 1John 5: 11-12

Kukhala mwana wa Mulungu ndi chinthu chimene inu munga tsimikize. Sichidalira pa momwe mumvera mthupi mwanu chifukwa simukhala chimodzi modzi nthawi zonse. Nthawi zina mumakhala okondwa kwambiri ndipo zina siziritero. Koma kutsimikiza chipulumutso chanu sichidalira pa momwe mumvera chidalira pachina chake chodalilika kopambana. Muphunziro iri mudzadziwa mutu wa chitsimmikizo chimenechi. Mzimu Woyera akuunikileni m'nzeru zanu ndi kulimbitsa chikhulupililo chanu pomwe muku werenga phunziro iri.

NDIDZIWA KUTI NDINE MWANA WA MULUNGU KUPITIRA MUMALONJEZO A MAWU A MULUNGU

1. Werengani Chibvumbulutso 3:20. Mau akuti Ngati tiitana Khritu mumtima mwathu iye adza bwela mwa iye.
   - Kodi muna mu pempha kuti a lowe mu mtima mwanu?_____
     _____
   - Kodi Khristu alikuti tsopano?_____

2. Werengani Yohane 1:12
   - Potsata malemba awa, kodi iwo amene amalandira Khristu asanduka yani? _____
   - Kodi mutsimikidiza kuti munalandira Khristu ndi kukhulupilira iye?
     _____
   - Potsata zimenezo, kodi ndinu mwana wa yani tsopano?_____
     _____

3. Werengani 1 Yohane 5:13
   - Kodi tinga tsimikize motani kuti tiri ndi moyo wosatha?_____
     _____

NDIDZIWA KUTI NDINE MWANA WA MULUNGU CHIFUKWA CHA NKHALIDWE NDI UMBONI WAMZIMU WOYERA

4. Welengani 1Yohane 3:24
   - Kodi tidziwa bwanji kuti Khristu akhala mwa ife?_____
     _____

5. Werengani Aroma 8:16
   - Kodi tidziwa bwanji kuti ndife ana a Mulungu? _____
     _____

NDIDZIWA KUTI NDINE MWANA WA MULUNGU CHIFUKWA CHAKUSINTHA KWA UMOYO WANGA WATSOPANO

6. Werengani 1 Yohane 2: 3-6
   - Kodi ndi dalira pa chiani ponena kuti ndimdziwa Mulungu?(ndime3)
     _____
   - Kodi tinga tsimikize bwanji kuti wina wache akunama kapena kunena choonadi kuti amdziwa Mulungu? _____
     _____

- If we claim to know God, but we are not keeping His commandments, what are we? (ndime 4) _____

NDIDZIWA KUTI NDINE MWANA WA MULUNGU CHIFUKWA CHA MOMWE NDIKHALIRA NDI ENA

7. Werengani 1 Yohane 3:14 -15
   - Kodi tidziwa kuti bwanji kuti tachoka mu imfa kulowa mu umoyo? _____
   - Kodi Yohane amucha yani amene sakonda mbale wake? _____ _____
   - Kodi ali nao moyo wosatha?_____

NDIDZIWA KUTI NDINE MWANA WA MULUNGU CHIFUKWA CHA MOMWE NDIONERA CHIMO MU UMOYO WANGA

8. Werengani 1 Yohane 3 :4-10. Mundime izi, liu loti chimo litanthauza uchimo wochita dala. Si zolakwa zomwe timachita mosayembekezera kuchita.
   - Kodi chimo dichiani (ndime 4) _____
   - Kodi Yesu anadza padziko pano kudzatani?(ndime 5) _____ _____
   - Kodi Yohane akuti bwanji ponena za munthu okonda uchimo ? (ndime 6) _____
   - Kodi tingamdziwe bwanji munthu wolungma?(ndime 7) _____ _____
   - Kodi munthu wa umoyo wa uchimo ndi wayani?(ndime 8) _____ _____
   - Kodi nkotheka kuti munthu angapitilize ndi uchimo ndi kumatinso ndi wo badwa mwa Mulungu?(ndime 9)_____ _____
   - Kodi tingatsimikize bwanji ana a Mulungu ndi ana a Satana?(ndime 10) _____

9. Werengani 1 Yohane 2:1
   - Kodi ndi chifukwa ninji Yohane analemba zinthu izi? _____
     _____

10. Werengani 1 Yohane 1:9
   - Ngati tagwa m'chimo tifunika kuchita chiani mosachedwa? _____
     _____
   - Ngati tilapa machimo athu kwa Mulungu chimachitika ndichiani?
     _____

Ngati mwalakwa ndi ku kwiitsa Mulungu muyenera kulapa kwa iye pompo ndi kupempha chikhululukiro. Mupemphe thandizo lo gonjetsera khalidwe loipalo ndi kuyamba umoyo wa tsopano. Mulungu afuna kuti inu mukhale ndi umoyo wa ngwiro osati wa uchimo

MAFUNSO A ZOKAMBIRANA

1. Kodi Mzimu Woyera amagwira nchito yotani po zachitsimikizo cha chipulumutso changa?

2. Kodi umboni wo onetsera poyera kuti ndina sandukadi mwana wa Mulungu.

3. Kodi ndingati ndine mwana wa Mulungu ngati ndi pitiliza kuchimwira dala?

Lembani ndime yapa ntima apa 1 Yohane 5 :11-12

_____
_____
_____
_____
_____

Kodi Chipulumutso ndi chiani ?



Kuyenda ndi Mulungu

2

Eph 2 *[1]Ndipo inu, anakupatsani moyo, pokhala munali akufa ndi zolakwa, ndi zochimwa zanu, [2]zimene munayendamo kale monga mwa mayendwe a dziko lapansi lino , monga mwa mkulu wa ulamuliro wa mlengalenga , wa mzimu wakuchita tsopano mwa ana a kusamvera; [3]amene ife tonsenso tinagonera pakati pao kale , kale muzilakolako za thupi lathu , ndi za maganizo ,ndipo tinali ana a mkwiyo chibadwire, monganso otsalawo; [4]Koma Mulungu wolemera chifundo, chifukwa cha chikondi chache chachikuru chimene anatikonda nacho, [5]tingakhale tinali akufa muzolakwa zathu, anatipatsa moyo pamodzi, ndi Khristu (muli opulumutsidwa ndi chisomo), [6]ndipo anatiukitsa pamodzi, natikhazikitsa pamodzi ndizakumwamba mwa Khristu Yesu; [7]Kuti akaonetsere nyengo zirikudza chuma choposa cha chisomo chache, ndikukoma mtima kwa pa ife mwa Khristu Yesu. [8] Pakuti muli opulumutsidwa ndi chisomo chakuchita mwa chikhulupiriro, ndipo ichi chosachokerakwa inu: chiri mphatso ya Mulungu; [9]Chosachokera kunchito, kuti asadzitamandire munthu ali yense . [10]Pakuti ife ndife chipangano chache, olengedwa mwa krisu Yesu, kuchita nchito zabwino, zimene Mulungu anazipangiratu, kuti tikhale m'menemo.*

Lowezani: Aefeso 2 : 8-9

Mulungu ana konzera za chipulumutso dziko lisana khazikitsidwe. Yesu ana kwanilista chikonzero cha chipulumutso chathu kupyolera mu imfa yache pamtanda ndi ku ukitsidwa kwache kwa akufa . Choncho, chipulumutso simau chabe ai. Ndi choonadi chozizwitsa chomwe aliyense anga peze ngati alapa machimo ake ndi kulandila Yesu Khristu mchikhulupiliro.
Muphunziro ili mudza phunzira zina zazinthu zoposa zomwe zinachitika pomwe inu machikhuluphiriro muna mlandira Yesu mumtima mwanu.

MACHIMO ANU ANAKHULUKIDWA

1. Werengani Yohane 3:16
   - Kodi ndichifukwa ninji Mulungu ana tumiza mwana wache pa dziko lapani? _____
   - Kodi pamene inu munakhulupirira mwa Khristu munalandira chiani? _____

2. Werengani 1 Yohan1:9
   - Kodi Mulungu anachita chiani pamene inu muna lapa machimo anu kwa iye?_____

3. Werengani Ntchito 3:19
   - Kodi ndichiani chinachitika kumachimo anu pamene muna tembenuka?_____

4. Werengani Akolose 1:14
   - Kodi chiombolo ndi chikhulukiro chanu china konzeredwa motani? _____

5. Werengani Ahebri 10:17
   - Kodi a mbuye adzakumbukiranso machimo anu?_____ _____

MULUNGU ANA KULUNGAMITSANI

6. Werengani Yohne 3:17-19
   - Ndichifukwa ninji anthu aweruzidwa kapena kupezedwa ndimlandu pamaso pa Mulungu? _____

7. Werengani Yohane 3:18
   - Kodi tichitenji kuti tisaweruzidwe?_____

8. Werengani Aroma 5: 1
   - Kodi ndi chiani chitsatira kulungamtsidwa mwa chikhulupiriro ?____ _____

9. Werengani Aroma 8:1
   - Ndi ndani kodi amene ali omasulidwa kuchiweruzo ? _____ _____

MUNABADWA KACHIWIRI NDI KUKHALA A MOYO MUMZIMU

10. Werengani Yohane 3:3-7

[3]Yesu anayenkha nati kwa iye.Indetu,indetu,ndinena ndi iwe, Ngati munthu sabadwa mwatsopano, sakhoza kuona ufumu wa Mulungu
[4]Nikodemo ananena kwa iye, munthu akhoza bwanji kubadwa atakalamba? Kodi akhoza kulowanso m'mimba ya amache ndi kubadwa nso kachiwiri?
[5]Yesu anayankha, "Indetu, indetu , ndinena ndi iwe, ngati munthu sabadwa mwa madzi ndi Mzimu, sakhoza kulowa ufumu wa Mulungu [6]Chobadwa mthupi chikhala thupi, ndipo chobadwa mwa Mzimu , chikhale Mzimu. [7]Usadabwe chifukwa ndinati chifukwa ndinati kwa iwe: Uyenera kubadwa mwatsopano.

- Ndi chifukwa chiani tiyenera kubadwa kachiwiri? _____

11. Werengani Efezo 2:1-5
- Kodi munali otani Mulungu asanakuukitseni?_____
_____

12. Werengani Yohane 5:24
- Ndi chiani chomwe mulinacho tsopano chomwe munalibe kalero?
_____

13. Werengani 2 Akorinto 5:17
- Kodi munthu yemwe ali Mwa Khristu Yesu achedwa otani?
_____
_____

MUNASANDU TSI DWA MWANA WA MULUNGU

14. Werengani Yohane1:12
- Kodi yense amene wa landira Yesu Khristu amapatsiddwa mphamvu zotani?_____
_____

15. Werengani 1 Yohane 3:1-2
- Kodi titchedwa yani tsopano chifukwa cha chikondi choposa cha Mulungu ?
_____
_____

16. Werengani Aroma 8:14
- Kodi chimodzi chazizindikiro chakuti ndife ana a Mulungu ndi chotani?_____
_____

17. Werengani Aroma 8: 17

- Kodi olowa a Mulungu ndi ndani?_____

Chipulumutso ndi chinthu choposa ndiponso cho zizwitsa mdziko lonse lapani. Pali zambiri kupambana zomwe tayan'ganapo muphunziro iri. Chipulumutso chomwe tilinachochi ndichopitilirabe ndipo chidza peza kukwaniritsidwa kwache pa tsiku lodalitsika lija pamene ambuye adza bweranso.

Tito 2 *[11]Pakuti chaoneka chisomo cha Mulungu chakupulumtsa anthu onse. [12]ndi kutiphunzitsa ife kuti , pokakana chisapembedzo ndi zilakolako za dziko lapansi, tikhale ndi moyo mdziko lino odziletsa, ndi olungama, ndi opembedza; [13]akulindira chiyembekezo chodala,ndi maonekedwe a ulemerero wa Mulungu wamkuru ndi Mpulumutsi wathu Yesu Khristu ; [14]amene anadzipereka yekha mmalo mwa ife, kuti akatiombole ife ku zoipa zonse, nakadziyeretsere yekha anthu akhale ache eni eni, achangu pa nchito zokoma. [15]Izi lankhula, ndipo uchenjeze nudzudzule ndi ulamuliro, wonse. Munthu aliyense asakupeputse.*

MAFUNSO A ZOKAMBIRANA

1. Kodi Yesu Khristu ana konzera motani zachipulumutso chathu ?

2. Pelekani zitsanzo kuchokera Mu Baibulo ku onetsa momwe miyoyo ya anthu ina sinthila pamene ana pulumutsidwa?

3. Kodi mwasintha kotani kuchokera pomwe munalandira Khristu ngati mpulumutsi wanu?

Lembani ndime yo lowez a pa Aefezo 2:8-9

_____
_____
_____
_____
_____

Pemphero

Kuyenda ndi Mulungu
3

Mateyu 27 *[45]Ndipo ora lachisanu ndi chimodzi panali mdima pa dziko lonse, kufikira ora lachisanu ndi chinai [46]ndipo poyamdikira ora lachisanu ndi chinai, Yesu anapfuula ndi mau akuru, kunena, Eli, Eli, lama sabakitani? Ndipo kuena kuti, Mulungu wanga, Mulungu wanga, mwandisiyiranji ine? [47]Nipo ena a iwo akuimirira komweko, pamene anamva, ananena, Uyo aitana Eliya. [48]Ndipo pomwe mmodzi wa iwo anathamanga, natenga chinkhulupule nachidzadza ndi vinyo wosasa, nachiika pabango, namwetsa Iye. [49]Koma ena anati., "Taleka , itione ngati Eliya adzafika kudzampulumutsa." [50] Ndipo Yesu, pamene anapfuula ndi mau akuru, anapereka mzimuwache. [51]Ndipo onani, chinsaru chochinga cha mkachisi chinang'ambika pakati, kuchokera kumwamba kufika pansi; ndipo dziko linagwendezeka, ndi miyala inan'gambika; [52]ndi manda anatseguka, ndi mitembo yambiri ya anthu oyera mtima, akugona kale, inauka; [53]ndipo anaturuka m'manda mwao pambuyo pa kuuka kwache, nalowa m'mzinda woyera, naonekera kwa anthu ambiri. [54]Ndipo pamene mkuru a wa asilikari, ndi iwo anali naye akudikira Yesu, anaona chibvomezi, ndi zinthu zimene zinachitidwa, anaopa kwambiri, nanena, Indedi Uyo ndiye Mwana wa Mulungu .*

Mchipangano chakale anthu sanalikutha kulowa mu kachisi. Ansembe okha ndiwo analoredwa kulowamo, ndipo ndi mkulu wa ansembe yekha amene analoredwa kulowa kumbuyo kwa chinsalu cho chinga ndikulankhula ndi Mulungu. Koma pamene Yesu anafela machimo athu, anachotsa ukali wa Mulungu. Tsopano anthu onse atha kukhulukilidwa ndi kulankhula naye Mulungu. Nchifukwa chake chinsalu cho chinga chamkachisi chija china ng'ambika pakati. Mulungu anali kutiitana ife kuti tibwele ndi kulankhula naye. Sikusowekanso kuti ife tilankhule ndi Mulungu ku pitila mwa wa nsembe.

MULUNGU ATI ITANA IFE KUTI TIPEMPHERE

1. Werengani Yohane 16:24
   - Ubale wathu ndi Mulungu umakula ngati ife tipenphera. Kodi ngati tipemphera chimachitika ndi chiyani?_____

2. Werengani Mateyu 7:7
   - Ndichiyani chomwe Mulungu afuna kutichitira pomwe tipemphera kufuna ndi kugogoda?_____

3. Werengani Mateyu 26:41
   - Kodi chifukwa china chomwe ife tifunika kupemphera ndi chiti? _____
     _____

4. Werengani Luka 11:1-4
   - Ndi zinthu zotani zomwe tiyenera kupempherera? _____
     _____

UMOYO WOPEMPHERA KAWIRI KAWIRI

5. Werengani Marko 1:35 ndipo taonani chitsanzo chomwe Yesu anapereka pa Kupempherea
   - Kodi amapemphera nthawi yanji?_____
     _____

6. Werengani Luka 6: 12-16
   - Kodi mpemphero unali ofunika motani kwa Yesu? _____
     _____

7. Werengani Luka 10: 38-42
   - Marita anali kugwira nchito ndi mphamvu, koma Maria anali kuchita chinthu choposa apo. Kodi Maria anali kuchita chiani? _____
     _____
   - Kodi kukhala pamapazi a Yesu kufanana bwanji ndi Kupemphera?
     _____

KAPEMPHEREDWE

8. Werengani Luka 18:9-14
   - Nchifukwa ninji Yesu sanalikonde pemphero lamfarisi?_____

- Kodi Mulungu analikonderanji pemphero la munthu wachiwiriyo?

_____

9. Werengani Mateyu 6: 5-8
   - Kodi Yesu ati uza kuti tipemphere motani?_____

10. Werengani Machitidwe 4:31
    - Kodi mndime iyi, Ophunzira anali kuti pamene anapemphera? _____

_____

Nthawi zina timapemphera tokha, nthawi zina pamodzi ndi anzathu. Kulibe njira imodzi yomwe tinga pempherereremo koma chosowekera kwambiri nchakuti ife tikhale ndi mtima odzichepetsa pomwe tilankhula ndi Mulungu.

11. Werengani Aroma 8:26-27
    - Mulungu amatithandiza motani pamene sitidziwa mau ogwiritsa nchito popemphera? _____

PEMPHERO LOYANKHIDWA

12. Werengani Yohane 15:7
    - Tichitenji kuti maphemphero anthu ayankhidwe? _____

_____

13. Werengani Mateyu 21:21-22
    - Kodi pemphero iri ndi mphamvu zotani? _____

_____

Anthu ena amasokonezeka pomwe Mulungu akana kuyankha mapemphero awo. Kuli zina zache zosowekera kuti mapemphero ayankhidwe.

14. Werengani Mateyu 26:39
    - Nichiani chomwe Yesu sanafune kuti chichitike?_____

    - Koma anafunitsitsa chiani kupambana chomwe ana pempha?_____

_____

15. Werengani 2 Akonrito 12:7-9
    - Ndi chifukwa chiani pemphero la Paulo siri nayankhidwe?_____

_____

16. Werengani Yakobo 4:1-3

- Ndi chifukwa chiani maphemphero a aKhristua awa sayankhidwa?

_____

Tilimbitsidwa kumphempha Mulungu zomwe tifuna koma tiyenera kukhala ogonjera kufuna kwache m'mapemphero athu. Pamene tikula mkuvetstsa kwathu za njira za Mulungu, tidza phunzira kudziwa mapemphero omwe akonderesta Mulungu.

17. Werengani Mateyu 6:33

- Chimene chiyenera kukhala chofumikira kwambiri pamene tipempherera ndi chiyani? _____

MAFUNSO AZOKAMBIRANA

1. Ndima pemphero otani omwe Mulungu adzayankha nthawi zonse? Ndimapemphero otani omwe iye sadzayankha?

2. Mulungu anang'amba chinsalu cho chinga cha mukachisi ndi kutiitana ife kuti tibwere ndi kulankhula naye. Kodi tiku mutukwana iye ngati ife sitifuna kupemphera.

3. Mulungu ndi wamphamvu kupambana mtsogoleri wadziko lililonse. Kodi mtsogoleri wadziko lanu ata kuitananani kuti mumuuze zosoweka zanu, mudza tero kodi? Kodi ife sitiyenera ukhala okondwa kwambiri kumuuza Mulungu zo soweka zathu? Muganizo kuti nchifukwa ninji ena amalephera kupemphera?

Lembani ndime yo loweza: Mateyu 7:7

_____
_____
_____
_____
_____

Kuwerenga Baibulo

Kuyenda ndi Mulungu

4

Yohane 15 *[1]Ine ndine mpesa weniweni, ndipo Atate wanga ndiye wamunda. [2]Nthambi iri yonse ya mwa ine yosabala chipatso, aichotsa; ndi iri yonse yakubala chipatso, aisadza, kuti ikabale chipatso chochuruka. [3]Mwakhala okonzeka tsopano inu chifukwa cha mau amene ndalankhula ndi inu [4]Khalani mwa Ine, ndi Ine mwa inu. Monga nthambi siingathe kubala chipasto pa yokha, ngati siikhala mwampesa; motere mulibe inunso gati simukhala mwa ine.*

[5]Ine ndine mpesa, inu ndinu nthambi zache: wakukhala mwa ine, ndi ine mwa iye , ameneyo abala chipasto chambiri; pakuti kopanda Ine simungathe kuchita kanthu. [6]ngati wina sakhala mwa iye, watayika kunja monga nthabi, nafota; ndipo azisonkhanitsa nazitaya kumoto, nazitentha. [7]Ngati mukhala mwa Ine, ndi mau anga akhala mwa ine, pemphani chimene chiri chonse mufuna ndipo chidzachitika kwa inu. [8]Mwa ichi alemekezedwe Atate wanga, kuti mubale chipatso chambiri; ndipo mudzakhala akuphunzira anga. [9]Monga momwe Atate wandikonda Ine, Inenso ndakonda inu; khalani muchikondi changa. [10]Ngati musunga malamulo anga mudzakhala muchikondi changa; monga Ine ndasunga malamulo a Atate wanga, ndipo ndikhala muchikondi chache. [11]Izi ndalankhula ndi inu, kuti chimwemwe changa chikhale mwa inu, ndi kuti chimwemwe chanu chidzale.

Lowezani: Yohane 15:10

Mwana akabadwa nkofunika kusamala kuti apitilize kukhala ndi moyo ndiponso kukula. Chimodzi modzi ndi umoyo wachi Khristu. Pamene tikhala ana a Mulungu tiyenera kupitiliza kukhala ngati ana a Mulungu ndinso kukula. Chimakondweletsa atate athu akumwamba ngati ife tikula komanso ngati tikhulupirira. Muphunziro izi tidzaona zina zazinthu zimene muyenera kuchita kuti muthandizadwe kukula muchiKhristu chanu.

BAIBULO NDI MAU AMULUNGU KWAIFE

1. Werengani 2 Timoteo 3: 14-17
   - Kodi kuwerenga Baibulo kuna mpindulira motani Timoteo? (ndime 15)
     _____
   - Kodi Baibulo inachokera kuti? (ndime16)_____
     _____
   - Kodi malemba ndi abwino motani? (ndime 17)
     (a)_____
     (b)_____
     (c)_____
     (d)_____
   - Kodi malemba ama mchitira chiani munthu wa Mulungu? (ndime 17) _____

2. Werengani 2 Petro 1:19-21
   - Petro atiuza kuti Baibulo ili ngati muuni aku unika mumdima. Kodi titani nao? (ndime19)_____
     _____
   - Kodi Baibulo inachokera kuti?_____

3. Werengani Mateyu 5:18
   - Kodi Baibulo limasintha?_____

Choncho tidziwa kuti Baibulo lichochera Kwa Mulungu. Ndi mau a Mulungu kwa ife. Ndi njira imodzi yomwe Mulungu amalankhula ndi ife lero. Tidziwanso kuti titha kukhulupirira kuti pazaka zapita zambiri Baibulo silinasinthe.

4. Werengani Machitidwe 17:11
   - Kodi nchifukwa ninji anthu aku Berea ana lingaliridwa kukhala afulu?
     _____
     _____

5. Werengani Aroma 15:4
   - Nchifukwa chiani Baibulo ina lembedwa?_____
     _____

KUWERENGA NDI KULOWEZA MAU A MULUNGU KAWIRI KAWIRI

6. Salimo 119:11 ikuti Ndabisa mau anu mumtima mwanga kuti ndisa kuchimwireni
   - Munga pereke chitsanzo momwe mau a Mulungu adzakutetezani ku uchimo?_____
     _____

7. Werengani Yohane 15:7
   - Tichitenji kuti maphemphero athu ayankidwe?_____
     _____

8. Salimo 119: 105 Mau anu ndi nyali ya mapazi anga muuni wa njira yanga.
   - Mau a mulungu alibwanji ngati muuni kwa inu?_____
     _____

9. Werengani 1 Yohane 5: 13
   - Kodi kuwerenga Baibulo kuli ndi phindu lotani?_____
     _____

KUPITILIZA KUNVERA NDI KUKHULUPIRIRA MULUNGU KO THERATU

10. Werengani Yohane 15:9-15
    - Tipitilize kuchita chiani kuti tikhale mchikondi cha Yesu?_____
      _____
    - Kodi Yesu watizindikiritsa chiani ?_____
      _____

11. Werengani 1 Yohane 1 :7
    - Chifunika ndichiyani kuti M'Khristu a pitilize kuyanjana ndi Mulungu ndi kutsukidwa ku machimo onse?_____
      _____

12. Werengani 2 Timoteo 4:7
    - Ndi chiani chimene Paulo anadziwa?_____
      _____

13. Werengani Aroma 12:1-2
    - Ngati mwadzi pereka kwa Mulungu ndi ku santhula Baibulo mu madzadziwa njira zache. Ndichiani chomwe Paulo akuti chimasintidwa?
      _____

MAFUNSO A ZOKAMBIRANA

1. Baibulo inalembedwa panyengo ya zaka zo pyola mazana awiri (2000) kuchokera nthawi ya Mose mpaka mpostoli womaliza. Olemba anali ndi maphunziro osiyana siyana ndiponso zomwe ana oona mu umoyo, koma ndi Mzimu Woyera yemweyo ekha amene anawa tsogorera onsewo. Kodi mutha kuona kuti khalidwe la a lembi osiyana lionekera mzoremba zao? Mukuonanso kuti angakhale ziri tero uthenga susintha ai?

2. Kodi kudziwerengera Baibulo pa ife tokha kumatithandiza bwanji mkukula kwathu muchiKhristu?

MAGANIZO AMENEWA MUNGAYENDETSERE UMOYO WANU WA UZIMU

Tsiku lili lonse muyenera kupeza nthawi yowerenga Baibulo ndi kulankhula ndi Mulungu m'mapemphero mupeze, ngati nkotheka, malo ndi nthawi pomwe inu mungakhale panokha ndiponso chete. Chingakhale cha bwino kuyamba kuwerenga uthenga wa Yohane. Patsiku lililonse muwerenge mutu umodzi ndi kumatenga nthawi yo lingalira chimene zomwe mwawelenga zitanthauza kwainu. Mulungu afuna Kulankhula nanu mu mau ake. Nthawi zambiri chimathandiza kukhala ndi kabukhu kolembamo maganizo ndi mafunso amene abwera kwainu pamene muli kuwerenga.

Mutamaliza kuwerenga, mukhaleko ndi nthawi yo pemphera. Muyambire kuthokoza Mulungu pa zomwe mwa werenga. Mumthokoze chifukwa chikondi chake ndi madalitso ache ambiri. Pemphererani banja lanu, anzanu ndi onse amene asanaphulumutsidwe. Mudzipempherere nokha kuti Mulungu akuthandizeni mu umoyo wanu wachi Khristu . Mfotokozereni za mabvuto ali onse amene muli nao ndi kumphempha kuti aku thandizeni kumdziwa bwino.
Umoyo wanu wa uzimu tsiku ndi tsiku m'dzakhala muKhristu wolimba.

Lembani ndime yo loweza Yohane 15:10

Kuuzaena

Kuyenda ndi Mulungu
5

Yohane 4 *[4]Ndipo anayenera kupita pakati pa Samariya. [5]Chifukwa chache anadza ku madzi wa Samariya, dzina lache Sakari, pafupi pa dziko kamene Yakobo adapatsa mwana wache Yosefe; [6]ndipo pamenepo panali chitsime cha Yakobo. Ndipo Yesu, popeza analema ndi ulendo wache, motero anakhala pacitsime. [7]Kunali ngati ora lachisanu ndi chimodzi. Kunadza mkazi woturuka msamariya kudzatunga madzi. Yesu ananena naye, " Undipatse Ine ndimwe. [8]Pakuti ophunzira ache adachoka kunka kumudzi kuti akagule chakudya.*

[9]Pamenepo mkazi wa msamariya ananena ndi Iye, "Bwanji Inu, muli Myuda, mupempha kwa ine kumwa, ndine mkazi Msamariya?" (pakuti Ayuda sayenderana nao Asamariya). [10]Yesu anayankha nati kwa iye, "Ukadadziwa mtulo wa Mulungu , ndi Iye amene alinkunena ndi iwe, Undipatse Ine ndimwe; ukadapempha Iye, ndipo akadakupatsa madzi amoyo."

[11]Mkaziyo ananena ndi Iye, Ambuye, mulibe chotungira madzi, ndi chitsime chiri chakuya; ndipo mwatenga kuti madzi amoyo? [12]Kodi muli wamkuru ndi atate wathu Yakobo amene anatipatsa ife chitsimechi, ndi zoweta zache?
[13]Yesu anayankha nati kwa iye, Yense wakumwako madzi awa adzamvanso ludzu; [14]Koma iye wakumwa madzi amene Ine ndidzampatsa sadzamvaludzu nthawi zonse; Koma madzi amene Ine ndidzampatsa adzakhala mwa iye kasupe wa madziotumphukira ku moyo wosatha.[15] kapena ndisadze kuno kudzatunga.

[16]Yesu ananenakwa iye ,muka kumuitane mwamuna wako,nudze kuno. [17]Mkazi anayankha nati kwa Iye, Ndiribe mwamuna. Yesu ananena naye, Wanena bwino, kuti mwamuna ndiribe; [18]pakuti wakhala nao amuna asanu; ndipo iye amene ukhala naye tsopano sali mwamuna wako; ichi wanena zoona. [19]Mkazi ananena ndi Iye, Ambuye, ndizindikira muli Mneneri. [20]Makolo athu analambira mphiri ili; ndipo inu munena , kuti mYerusalem muli malo oyenera kulambiramo anthu.

[21]Yesu ananena naye, Tamvera Ine, mkazi iwe, kuti ikudza nthawi, imene simudzalambira Atate kapena mphiri ili, kapena m Yerusalemu. [22]Inu mulambira chimene simudzalambira ife tilambira chimene tichidziwa; pakuti chipulumutso chichokera kwa Ayuda. [23]Koma ikudza nthawi,ndipo tsopano iripo,imene olambira oona adzalambira Atate mumzimu ndi mchoonadi; pakuti Atate afuna otere akhale olambira ache. [24]Mulungu ndiye mzimu; ndipo omlambira Iye ayenera kumlambira mumzimu ndi choonadi.

[25]Mkazi ananena ndi Iye Ndidziwa kuti Mesiya adza (wotchedwa Khristu): akadzadza Iyeyu,adzatuiza zonse.
[26]Yesu ananena naye, Ine wakulankhula nawe ndine amene.
[27]Ndipo pamenepo anadza ophunzira ache; nazizwa kuti analinkulankhula ndi mkazi; koma panalibe wina anati, Mafuna chiani? Kapena, mulankhula naye chiani?
[28]Pamenepo mkazi anasiya mtsuko wache, namuka kumudzi, nanena ndi anthu,
[29]Tiyeni mukaone munthu, amene anandiuza zinthu ziri zonse ndinazichita: ameneyu sali Khristu nanga?
[30] Anaturuka iwo mumudzi ndipo analinkudza kwa Iye.

[39]Ndipo mumudzi muja anthu Asamariya ambiri anamkhulupirira Iye chifukwa cha mau a mkazi, wochita umboniyo,kuti, Anadiuza ine zinthu ziri zonse ndinazichita.

Lowezani: Machitidwe 1:8

Monga momwe mzimai wa ku Samaria anakauzako anzake za Yesu, ifenso teyenera ku uzako ena. Pamene ana pempherera ophunzira ake kwa atate ake, Yesu anati, ÒIwo sia dziko lapansi monga ine sinili was dziko lapansi. Monga inu Munandi tuma mudziko lapansi ndawa tuma mudziko lapansi. Ndife otumidwa ku chitira umboni wa Khristu padziko lapansi kuti iwo amkhulupirireiye. Kuchitira umboni ndi kufotokofa zimene Yesu anali kuchitira inu-momwe wa sinthila moyo wanu. Tiri ndi chinthu cho ziswitsa chomwe tinga nawo anzathu.

DZIKO LAPANSI LIFUNIKA KUMVA UTHENGA

1. Werengani Aefeso 2:12
   - Kodi mau awa afotokoza motani za iwo amene sanabadwe kachiwiri?_____
     _____
2. Werengani Yohane 3:18
   - Kodi kuweruzidwa kudza chifukwa ninji?_____
     _____
3. Werengani Luka 19:10
   - Kodi nchifukwa ninji Yesu anadza padziko lapansi? _____
     _____
4. Werengani Yohane 3:16
   - Kuti apulumuke anthu ayenera kuchita chiani? _____
     _____
5. Werengani Yohane 14:6
   - Kodi kupatulako kukhulupilira Yesu, kuli njira zina zomwe munthu anga pulumukiremo?_____

AKHRISTU AYENERA KUBWERETSA ANTHU KWA KHRISTU

6. Werengani Yohane 1:40-42
   - Atayamba ku tsatira Yesu Andrea achita chiani?_____
     _____

7. Werengani Yohane 1:42
   - Kodi Andrea anambweretsa kwayani Simoni?_____
     _____

8. Werengani Luka 8:39 Atachiritsidwa munthu uja anali odzazidwa ndi ziwanda,
   - Kodi Yesu ana mutuma kuti ? _____
   - Kodi Yesu amawauza kuti akachite chiani ?_____
   - Ndikuti kwina komwe munthu yu anafotokoza za Yesu ?_____

9. Werengani Machitidwe 1:8
   - Kodi Yesu afuna kuti ife tichite chiani titalandira mphamvu?_____
     _____
   - Tidzakhala nazo mphamvu zo chitira umboni kodi mphamvuzi zifuma kuti? _____

10. Werengani Yohane 4:7
    - Kodi Yesu anapereka umboni kwa anthu angati? _____

11. Werengani Machitidwe 8: 26-39
    - Ndikwa yani komwe Filipo ama pereka umboni? _____

12. Werengani Machitidwe 5: 42
    - Ndikuti kumene ophunzira a Yesu ana phunzitsa ndi kulalikira?_____
      _____

MZIMU WOYERA APATSA MPATSO ZAPADERA ZO GWIRIRA NTCHITO

13. Werengani Akorinto 12: 4-11
    - Kodi mphasto zotani zomwe zimathandiza popereka umboni?____
      _____

14. Werengani Aroma 12: 3-8
    - Ndimphasto zotani zomwe zi chulidwa apa?
      _____
      _____

15. Werengani 1 Akorinto 12:11
- Kodi aliko aKhristu amene alibe mphasto ? _____

16. Werengani Aefeso 4: 11-13
- Kodi ndi nchito yanji imene mphatso ziyenera kugwira? _____
_____

LINGO LANGA PA ZAKU CHITIRA UMBONI

17. Lembani maina a anthu atatu amene mudza wa pempherera ndi ku wa chitiraumboni_____
_____
_____

18. Lingarirani mumene mudza fotokozera zimene Yesu wachita mu umoyo wanu. Lowezani mmene munga tsogolere wina mupemphero lo pempha chikhululukiro kwa Yesu .

MAFUNSO A ZOKABIRANA

1. Poyan'gana pazomwe mutha kuchita, mphatso zanzimu, ndi zomwe muna phunzira, ndi nchito yotani yomwe munga gwirlire ambuye.

2. Kodi nkosowekera kuti imuyo mu tsogolere anthu ena kwa Yesu?

3. Ndi ndani amene anaku bweletsani inu kwa Yesu? Pokhala inunso aKhristu tsopano, muyenera kuchita chiani?

Lembani ndime yo Loweza: Machitidwe 1:8

_____
_____
_____
_____
_____
_____

Kuyenda ndi Mulungu
6

Aroma 8 *[1]Chifukwa chache tsopano iwo akukhala mwa Khristu Yesu alibe kutsusidwa. [2]Pakuti chilamulo cha mzimu wa moyo mwa Khristu Yesu chandimasula ine ku lamulo la uchimo ndi la imfa. [3]Pakuti chimene chilamulo sichinathe kuchita, popeza chinafoka mwa thupi, Mulungu anatumiza Mwana wache wa Iye yekha chifanizo cha thupi la uchimo, ndi chifukwa cha uchimo, natsutsa uchimo mthupi; [4]Kuti choikika chache cha chilamulo chikakwaniritsidwe mwa ife, amene sitiyendayenda monga mwa thupi koma monga mwa mzimu.*

[5]Pakuti iwo ali monga mwa thupi asamalira zinthu za thupi; koma iwo ali monga mzimu asamalira zinthu za mzimu; [6]Pakuti chisamaliro cha thupi chiri imfa;koma chisamaliro cha mzimu chiri ndi moyo ndi mtendere. [7]Chifukwa chisamaliro cha thupi chidana ndi Mulungu ; pakati sichigonjaku chilamulo cha Mulungu pakuti sichikhoza kutero. [8]Ndipo iwo amene ali mthupi sangathe kukondweresta Mulungu.

[9]Koma inu simuli mthupi ai, koma mumzimu, ngatitu Mzimu wa Mulungu akhalabe mwa inu. Koma ngati munthu alibe Mzimu wa Khristu, siali wache wa Khristu. [10]Ndipo ngati Khristu akhala mwa inu, thupilo ndithu liri lakufa chifukwa cha uchimo; koma mzimu uli wa moyo chifukwa cha chilungamo. [11]Koma angati Mzimu wa iye amenen adaukitsa Khristu kwa akufa akhalabe mwa inu, Iye amene adaukitsa Khristu Yesu kwa akufa adzapatsanso moyo matupi anu akufa, mwa Mzimu wache wakukhala mwa inu.

Lowezani : A Efeso 5:8

Ndi anthu chokodweretsa ndithu ku khlulukilidwa machimo ndikukhala ndi mtendere ndi Mulungu. Komabe, palinso chinanso cho pyolerabe chomwe Mulungu afuna kukuchitirani inu. Afuna kukudzazani ndi Mzimu Woyera. Pamene Yesu ana choka pa dziko lino ndi kubwerera kwa atate ache, ana lonjeza kuti adza tumiza Mzimu Woyera kuti adzakhale nafe nthawi zonse. Mulungu afuna kukwaniritsa lonjezoli mu umoyo wanu. Nthawi zina ichi chimachedwa. Umoyo wodzazidwa ndi Mzimu Woyera. Tikango pulumutsidwa kumene kumachimo anthu timalandila Mzimu Woyera yemwe amatitsogolera muzoonadi za Mulungu ndipo amayamba nchito yakutisandutsa ngati Khristu. Pamene tidzazidwa ndi Mzimu Woyera, amati fikitsa pamalo a tsopano mkugomjetsa mu kuyenda kwanthu mchiKhristu. Amatipatsa mphamvu zomasulidwa ndinso mphamvu zothirira umboni wa Khristu.

MZIMU WOYERA AMAPATSIDWA KWA AKRISU

1. Werengani Yohane 16:7
   - Kodi Yesu analonjezanji kwa okhulupilira?_____
     _____

2. Werengani Aefeso 5:18
   - Kodi Mzimu Woyera akadzabwera adza chita chiani?_____
     _____

3. Werengani Yohane 16:8
   - Kodi Mzimu Woyera akadzabwera adz chita chiani?_____
     _____

4. Werengani Yohane 16:13
   - Nanga ina nchito ya Mzimu Woyera ndi yotani?_____
     _____

MZIMU WOYERA AMA TSUKA MTIMA

5. Werengani Machitidwe 15:8-9
   - Kodi Mzimu Woyera amatani nao mtima?_____
     _____

6. Werengani 1 Akonrinto 3 :1-3
   - Mau wa atiuza kuti mtima uyenera kutsukidwa, angakhale tita khulukilidwa kale machimo athu. Kodi aKorinto anali a Khristu otani?
     _____
     _____

7. Werengani 1Thessalonika 5:23
   - Kodi kutsuka kumeneku nkomalizika motani?_____
     _____

8. Werengani Aroma 6:6
   - Khalidwe lauchimo mumtima limachedwa munthu wakale. Kuona ndime iyi china chitika ndi chiani khukhalidwe lakhale ili?_____
     _____

9. Werengani Aroma 6:7
   - Ngati khalidwe lakale lafa chotsatira ndichiani?_____
     _____

10. Werengani Agalatiya 2:20
    - Pamene Paulo ana palichikidwa ndi Khristu ndani anali wa moyo mwa iye?_____

MZIMU WOYERA APATSA MPHAMVU

11. Werengani Machitidwe 1:8
    - Tidzalandila mphamvu pamene Mzimu Woyera titsikira ife. kodi mphamvu imeneji tidzailandira pa lingo lotani?_____
      _____

12. Werengani Machitidwe 4:31
    - Zotsatira kudzazidwa ndi Mzimu Woyera zinali zotani ? _____
      _____

13. Werengani Machitidwe 19:1-7
    - Kodi Paulo ana ona uti nkosowekera motani kuti tilandire Mzimu Woyera?_____
      _____

14. Werengani Agalatiya 5:22-23
    - Tika dzadzidwa ndi Mzimu Woyera mphatso zache zidzaonekera mu umoyo wathu. Lembani zinzindikiro zisanu ndi zinai zomwe zinga chedwe zipatso za Mzimu Woyera.

      _____
      _____
      _____
      _____
      _____
      _____

MAFUNSO A ZOKAMBIRANA

1. Zina za zipatso za mu umunthu ndi zotani? Agalatiya 5:19-21

2. Zipatso za Mzimu Woyera zidzaoneka bwanji muumoyo wathu?

3. Kodi anthu adza zindikira ngati mwa ife muli zipatso zaMzimu Woyera?

Zotsatira zaumoyo wo dzadzidwa ndi Mzimu Woyera ndi umoyo pambana ndi madalisto. Kodi mu makomana ndizokepheretsa mukafuna kumvera Khristu? Kodi ndina ndinu a mantha ndinso offoka muka chitira umboni? ngati nditero, izi ndi zizndikira zakuti mufunika kutsukidwa ndi ku dzazidwa ndi Mzimu Woyera.

Ngati mufunitsitsa umoyo udzazidwa mutha ku thandizidwa motere:

Pempherani: Vomerani lilakoloka chanu kuti mutsalidwe. Mudzi pereke wathunthu kwa Mulungu. Aroma 12:1-2 akuti Chifukwa chache ndikupemphani inu, abale, mwa zifundo za Mulungu kuti mupereke matupi anu nsembe yamoyo, yopatulika, yokondweretsa Mulungu, ndiko kupembedza kwanu koyenera. Ndipo musafanizidwe ndimakhalidwe a pansi pano; koma mukhale osandulika, mwa ku konzanso kwa mtima wanu, kuti muka zindikire chimene chiri chifuno cha Mulungu, chabwino, ndichokondweretsa, ndi changwiro.

Pemphani Mulungu kuti akudzazeni ndi Mzimu Woyera monga momwe ana konzera kuti adza chita. Aroma 6:19 akuti, Ndilankhula manenedwe a anthu chifukwa chakufoka kwa thupi lanu; pakuti monga inu munapereka ziwalo zanu zikhale akapolo a chilungamo kuti zichite chiyeretso.

Khulupirirani ndi kulandila Mzimu Woyera nthawi ino. Yamikani mulungu paku ku dzazani ndi Mzimu Woyera.

Lembani ndime yo loweza apa Aefeso 5: 18

_____
_____
_____
_____
_____
_____

Usungi Wa ChiKhristu



Kuyenda ndi Mulungu
7

Mateyu 6 *[19]Musadzikundikire nokha chuma pa dziko lapansi, pamene njenjete ndi dzimbiri zikononga; ndi pamene mbala ziboola ndi kuba. [20]Koma mudzikundikire nokha cuma m'mwamba pamene njenjete kapena dzimbiri sizikononga, ndipo mbala siziboola ndi kuba;[21]pakuti kumene kuli chuma chako, komwe udzakhala mtima wakonso.*

[22]Diso ndilo nyali ya thupi; chifukwa chache ngati diso lako liri la kumodzi, thupi lako lonse lidzakhala lowaritsidwa. [23]Koma ngati diso lako lirii loipa, thupi lako lonse lidzakhala lodetsedwa. Chifukwa chache ngati kuwala kumene kuli mwa inu kuli mdima, mdimawo ndiwaukuru ndithu! [24]Palibe munthu angathe kukhala kapolo wa ambuye awiri: pakuti pena adzamuda mmodziyo, ndikukonda winayo; pena adzakangamira kwa mmodzi nadzanyoza wina. Simungathe kukhala kapolo wa Mulungu ndi wa chuma.

[25]Nchifukwa chache ndinena kwa inu, musadere nkhawa moyo wanu, chimene mudzadya ndichimene mudzamwa; kapena thupi lanu, chimene mudzabvala. Kodi moyo suli woposa chakudya, ndi thupi loposa chobvala? [26]Ya ng'anirani mbalame zakumwamba kuti sizinafese ai, kapena sizimatema ai, kapena sizimatutira mnkhokwe; ndipo Atate wanu wa kumwamba azidyetsa. Nanga inu mulibe kusiyana nazo kuziposa kodi? [27]Ndipo ndani wa inu ndikudera nkhawa angathe kuonjezera pamasiku ache mkono umodzi? [28]Ndipo muderanji nkhawa ndi chobvala? Tapenyetsani maluwa a kuthengo, makulidwe ao; sagwiritsa nchito kapena sapota: [29]Koma ndinena kwa inu, kuti angakhale Solomo mu ulemelero wache wonse sanabvala monga limodzi la amenewa. [30]Koma ngati Mulungu abveka chotero maudzu a kuthengo, akhala lero, ndi mawa a ponyedwa pamoto, nanga si inu kopambana ndithu, inu akukhulupilira pang'ono? [31]Nchifukwa chache musadere nkhawa, ndi kuti, tidzadya chiani? kapena tidzamwa chiani? kapena tidzabvala chiani? [32]Chifukwa athu akunja azifuna zonse zimenezo; pakuti Atate wanu wa Kumwamba adziwa kuti musowazonse zimenezo. [33]Koma mthange mwa funa Ufumu wache ndi chilungamo chache, ndipo zonse zimenezo zidzaonjezedwa kwa inu. [34]Chifukwa chache musadere nkhawa za mawa; pakuti mawa adzadzidera nkhwa iwo wokha. Zikwanire tsiku zobvuta zache.

Lowezani: Aroma 12:1

ZONSE TIRI NAZO NZA MULUNGU

1. Werengani Akolose 3:1-4
   - Kodi Khristu alikuti tsopano? _____

- Mudzakhala kuti pamene Khristu adza onekera?_____

- Kodi maganizo athu akhale kuti?_____

2. Werengani Aroma 12:1
   - Muyenera kudzi ganizira motani tsopano?_____

3. Werengai 2 Akorinto 5:14-15
   - Umoyo wathu padziko lino lapansi ndiwa yani? _____

4. Werengani Agalatiya 2:20
   - Ndikhala yani mu moyo wanga? _____

Usungi wachi Khristu utanthauza kuti ife tizazindikira kuti Mulungu mwini wache weni weni wa umoyo wathu, uphatso zathu, nzelu zathu ndi chuma chathu chonse. Popeza kuti zonsezi zina chokera kwa iye, sizathu ai choncho ife tidza longosola kwa mmene takhalira ndi umoyo wathu ndi mmene tidza gwiritsa nchito zinthu zomwe tina patsidwazi.

Nzoona kuti pamene Yesu anatifera ife, tina sinthana naye malo. Ana tenga uchimo wathu ndipo ife tina tenga kulungama kwache. Tiri ndi umoyo wache ndipo iye ali ndi moyo wathu. Ngati inu ndinu aKhristu, moyo wanu siwanunso ai. Moyo wanu ngwache tsopano ndipo inu ndinu asungi chabe. Ndi chimodzi modzi ngati munthu amene a yang'anira sitolo yamwini. Sitolo ija syamusungi uja ndipo iye ayenera kulongosola kwa muwini sitolo.

MATUPI NDI MPHATSO ZATHU NZA MULUNGU

5. Werengani 1 Akonrinto 6:19-20
   - Ndani akhala mmatupi athu?_____

   - Kodi timlemekeza motani Mulungu?_____

6. Werengani Aroma 12:1
   - Tichite chiani ndi matupi athu?_____
     _____

7. Werengani Aroma 12:6-8
   - Tichite nazo chiani mphatso zomwe Mulungu anatipatsa?_____
     _____

8. Werengani Aefeso 5:16
   - Chinaso chomwe ife tiri asungi ndi chiani?_____

BAIBULO ITI UZA POYERA MOMWE TINGAYENDESTERE CUMA CHA MULUNGU

Chimodzi chizitsanzo zo yamba chipezeka mu Genesis 14:18-20.

9. Werengani Genesis 14:18-20
   - Kodi Abrahamu anamuyamika motani Mulungu? _____
     _____

Khalidweli lopeleka cha khumi pa zokolora zanu kwa mulungu china chedwa kuti CHA KHUMI. Ndi njira yomwe muma onestera kuti zonse nza Mulungu ndipo umoyo wanu udalira iye.

10. Werengani Genesis 28:20-22
    - Kodi Yakobo ana onetsa bwanji kuti anai ogonjera Mulungu?_____
      _____

11. Werengani Malachi 3:8-12
    - Ngati sitibweretsa chakhumi ndichiyani chomwe tiri kuchita kodi____
      _____
    - Ndi chiyani chima chitika ngati tipereka chakhumi kwa iwaridwa?___
      _____
    - Ndi chani chi machitika ngati tipereka cha khumi monga mmene kusowekera?_____

Yesu ana ona kupereka cha khumi ngati kanthu ka kang'ono ka zinthu zathu zimene ziri za mulungu.

12. Werengani Mateyu 23:23

- Kodi Yesu anakhulupirira kuti anthu ayenera kupereka cha khumi?
  _____
- Kupatulako cha khumi amanyembe kezeranso chiani?_____
  _____

13. Werengani Nehemiya 10: 37

- Ndizinthu zotani kupatulako ndalama zomwe tinga peleke cha khumi?
  _____

14. Werengani 2 Akorinto 9: 6-11

- Mulungu amandi thandiza bwanji kuti ndikhale ndi mtima wopatsa? (ndime 10)_____

MAFUNSO AZOKAMBIRANA

1. Kodi tingathe kupereka kupitilira pa cha khumi?

2. Zopereka zaufulu ndizo pereka zomwe zipitilila pa chakhumi. Zimenezi zitha kuperekedwa kuli konse komwe mufuna. Koma mukalibe katero Mulungu akuyembekezani kuti mupereke cha khumi kumpingo komwe mupemphera.Ndi mphatso zotani zomwe zinga khale zopereka zaufulu?

3. Ndi mnjira yotani momwe nkukoma mtima kwanu kwa anthu ena ku onetsa kuti muli kuthokoza Mulungu pa kukoma mtima kwake?

Lembani ndime yo loweza Aroma 12:1

_____
_____
_____
_____
_____

Kubvutika

Kuyenda ndi Mulungu

8

Yesaya 53 *[1]Ndani wamvera uthenga wathu? ndi mkono wa Yehova wabvumbulukira yani? [2]Pakuti ameneyo adzaphukira pamaso pache ngati muzu womera munthaka youma; Iye alibe maonekedwe, pena kukongola; ndipo pamene tiuona palibe kukongola kuti timkhumbe. [3]Iye ananyozedwa ndi kukanidwa ndi anthu; munthu wazisoni, ndi wodziwa zowawa; ndipo ananyozedwa monga munthu wombisira anthu nkhope zao; ndipo ife sitinamlemekeza.*

[4]Zoonadi Iye ananyamula zowawa zathu, ndi kusenza zisoni zathu; koma ife tinamuyesa wokhomedwa, wokanthidwa ndi Mulungu, ndi wobvutidwa. [5]Koma Iye analasidwa chifukwa cha mphulupulu zathu; chilango chotitengera ife mtendere chinamgwera Iye; ndipo ndi mikwingwirima yache ife tachiritsidwa. [6]Tonse tasochera ngati nkhosa; tonse tayenda yense mnjira ya mwini yekha; ndipo Yehova anaika pa Iye mphulupulu ya ife tonse.

[7]Iye anatsenderezedwa koma anadzichepetsa yekha osatsegula pakamwa pache; ngati nkhosa yotsogoleredwa kukaphedwa, ndi ngati mwana wa nkhosa amene ali du pamaso pa omsenga, motero sanatsegula pakamwa pache. [8]Anachotsedwa ku chipsinjo ndi chiweruziro; ndipo ndani adzafotozoka nthawi ya moyo wache? Pakuti walikhidwa kunja kuno; chifukwa cha kulakwa kwa anthu anga Iye anakhomedwa. [9]Ndipo anaika manda ache pamodzi ndi olemera mu imfa yache, ngakhale Iye sanachita chiwawa, ndipo mkamwa mwache munalibe chinyengo.

[10]Koma kunakomera Yehova kumtundudza; anammvesta zowawa; moyo wache ukapereka nsembe yoparamula, Iye adzaona mbeu yache, adzatanimphitsa masiku ache; ndipo chomkondweretsa Yehova chidzakula m'maja mwache.

Lowezani: 1 Petro 1: 6-7

Angakhale Yesu anali Mulungu mu umunthu, analorera kabvutika. Anabvutika pochoka ku mwamba, kukhala ngati m'mphawi padziko lapansi, kukanidwa ndi iwo anali azi bwenzi ache ndi kufa imfa yo wawa. Ichi anachitra dala, chifukwa anakonda aja ana sochela ndiponso anafuna kulemekezaa atate wache. Nthawi zina ichi chibvuta kumvesta kuti omkhulupitira aitanidwa kuyenda munjira yake.

YESU ANA BVUTIKA

1. Werengani Yesaya 53:3
   - Kodi umoyo wa padziko lapansi unali wa pafupi?_____

2. Werengani Luka 9:22
   - Kodi Yesu ana dziwa kuti adza bvutika?_____

3. Werengani Ahebri 12: 2-3
   - Nchifukwa ninji Yesu analola ku bvutika pamtanda?_____
     _____

TIDZA ZUZIDWA CHIFUKWA CHOTSATIRA YESU

4. Werengani 1 Petro 4:12-14
   - Kodi mabvuto atidabwitse ife?_____
   - Kodi chikondwelero chathu ndi liti?_____

5. Werengani Yohane 15:18-20
   - Kodi anthu ena zidzawakhubza motani akamva kuti ndinu m'Khristu?
     _____

6. Werengani Afilipi 1:29
   - Poonjezera umoyo womwe timalandila mwa Khristu tima patsidwanso chiani? _____
     _____

7. Werengani Luka 23:34
   - Yesu anawa yankha bwanji anthu omwe anamu pweteka? _____
     _____

Ifenso atiyembekeza kuyankha komwecho.

TITHA KUBVUTIKA MZOWAWA KAPENA MATENDA

8. Werengani Yohane 11:17-45
   - Kodi Yesu athakuchiritsa nthenda iri yonse?_____
     Inde ! Yesu ali ndi mphamvu yo chiritsa chirichonse. Komabe...

9. Werengani 2 Akorinto 12:7-10
   - Kodi Yesu amachiritsa nthawi zonse?_____

Ai! Chifukwa? Yesu sa chiritsa nthawi zonse chifukwa ali ndi lingo lopambana. Yesu si sing'anga winanso ai! Mphavu zache zipyola pamenepa. Ng'anga itha kuthandiza pang'ono chabe-koma Yesu ali kutipangila dziko lina lo chedwa kumwamba.

10. Werengani Chibvumbulutso 21:1-4
    - Ndiliti pamene Yesu adza chotsa kabvutika konse?_____
      _____

11. Werengani Yohane 14:1-4
    - Ndani amene Yesu adza pita nao ku mwamba?_____
      _____

Choncho, Yesu atha kutichiritsa koma cho sowekera kwambiri ndi kuti ife tikhale okonzeka kudzakhala mdziko latsopano lomwe ali kukonza.

12. Werengani Aroma 8: 28-29
    - Mulungu afuna kuti ife tifanane ndi yani?_____

Yesu anabvutika. Ngati simubvutika simungakhale ngati Yesu. Nchifukwa chake Paulo akuti Ndipo si chotero chokha, komanso tikondwerea mdzisautso; podziwa ife kuti chisautso chichita chipiriro; ndi chipiriro chichita chizolowezi; ndipo chiyembekezo sichitichititsa manyazi; chifukwa chikondi cha Mulungu chinatsandulidwa mmitima mwathu mwa Mzimu Woyera, amene wapatsidwa kwa ife. (Aroma 5: 3-5)

Yakobo akuti, Muchiyese chimwemwe chokha, abale anga m'mene mukugwa mumayesero a mitundu mitundu; pozindikira kuti chiyesedwe cha chikhuluphiriro chanu chichita chipiriro. Koma chipiriro chikhale nayo nchito yache yangwiro, kuti mukakhale angwiro ndi opanda chirema, osasowa kanthu konse. (Yakobo 1:2-4)

13. Werengani Aroma 8:18-19
    - Lofunikira kwambiri ndi liti, dziko lino lomwe lidzatha mosachedwa kapena la kumwamba limene silidzatha?_____

ZIFUKWA ZO BVUTIKIRA

14. Werengani Ahebri 12;7-11
    - Nthawi zina ku bvutika ndi kudzudzula kwa mulungu. Podzudzula Mulungu afuna ku chita chiani?_____
      _____

15. Werengani Yohane 9:1-5

- Nthawi zina Mulungu ati funsa ife ku limbikira angakhale pama bvuto. Mwa ichi tionetsa dziko lapansi kuti tili ndi chiyembekezo chopyola dzikoli. Yahane akuti timachitanji potereku?_____ _____Werenganinso Yohane 21:18-19

16. Werengani 1 Petro 5:8

- Kodi nthawi zina Mabvuto amadza ndi yani? _____

Ena amaganiza kuti matenda amadza chifukwa muli ndi uchimo mu moyo wanu. Zinga khale choncho Ndi zifukwa zambiri zomwe zinga bweretse mabvuto. Yesu ana bvutika koma analibe chimo. Nthawi zina ndi chifukwa chakuti Mulungu aku khulupirirani inu kotero aku pemphani kumvutikira iye.

17. Werengani Jakobo 5:13-16

- Kodi Mulungu afuna kuti tipempherere kuchiritsa?_____ _____

Indi chabwino ku pempha Mulungu kuti a chiritse koma tisa mu umirize. Khulupilirani iye. Ali ndi lingo loposa maganizo athu pa ife.

MAFUNSO AZO KAMBIRANA

1. Lingaurirani umoyo wa Yobu mchipangano chakale. Kodi ana bvutika chifukwa cha uchimo?

2. Chimene chifunika chikhuluphiriro cha mbiri ndi chiani : kukhala okondwa mmabvuto kapena ku chiritsidwa?

Lembani ndime yo loweza 1 Petro 1: 6-7

_____
_____
_____
_____
_____

Mpingo

Kuyenda ndi Mulungu

9

Machitidwe 2 *[41]Pamenepo iwo amene analandira mau ache anabatizidwa; ndipo anaonjezedwa tsiku lomwero anthu ngati zikwi zitatatu.*

[42]Ndipo anali chikhalire muchiphunzitso cha atumwi ndi muchiyanjano, kunyema mkate ndi mapempherero. [43]Koma panadza mantha pa anthu onse; ndipo zizindikilo zambiri zinachitika ndi atumwi. [44]Ndipo onse akukhulupira anali pamodzi , nakhala nazo zonse zodyerana [45]Ndipo zimene anali nazo, chuma chao, anazigulitsa, nazigawira kwa onse, monga momwe yense anasowera. [46]Ndipo tsiku ndi tsiku anali chikhalile ndi mtima umodzi mkachisi, ndipo ananyema mkate kunyumba kwao, nalandira chakudya ndi msangalalo, ndi mtima woona; [47]nalemekeza Mulungu, ndi kukhala nacho chisomo ndi anthu onse. Ndipo Ambuye anawaonjezera tsiku ndi tsiku amene akuti apulumustidwe.

Lowezani: Mateyu 16:18

Ife aKhristu tiri mbali yamgwirizano wa okhulupirira ochedwa mpingo. Mpingo utha kuchedwanso banja la Mulungu, ndi Mulungu ngati atate wathu wa kumwamba ndi aKhristu eni eni ena onse mdziko lapansi ngati azibale ndi azilongo athu. Mumgwirizano wa okhulupirirawu, tipezamo chikondi ndi chisamaliro. M'mgwirizano wa okulupirawu tipezamo chikondi ndi chisamaliro, chigwirizano ndi kupempedza kudyetsera ndi kugawana. M'bajali muli zisomo ndinso maudindo, ndipo ndi mbali imodzi yodabwitsa ya umoyo wa chiKhristu.

KHRISTU NDIYE MUTU WA MPINGO

1. Werengani Mateyu 16: 18
   - Kodi mpingo ndiwayani?_____
   - Ndani kodi amene adzamanga mpingo?_____

2. Werengani Aefeso 5:23
   - Mutu wa mpingo ndiye yani?_____

3. Werengani Aefeso 5:25
   - Kodi Khristu anauchitira chiyani mpingo?_____

MPINGO UCHEDWA THUPI LA KHRISTU

4. Werengani Aefeso 1:22-23
   - Kodi mpingo uchedwa chiani?_____

5. Werengani Aroma 12:5
   - Ngati ife ndife mbali ya thupi la Khristu pali ubale wotani pakati pa ife ndi aKhristu ena?_____

6. Werengani Aroma 12:10
   - Timva zotani kwa wina ndi mzache mthupi la Khristu?_____
     _____

7. Werengani 1 Akorinto 12:26
   - Timamva bwanji ngati A Khristu ena ali kupita m'mabvuto?_____
     _____
   - Timamva bwanji ngati A Khristu ena ali okondwera?_____
     _____

MPINGO UYENERA KUKULA NDI KUPITA PA TSOGOLO

8. Werengani Machitidwe 2:41-47
   - Mu ndime 41 ndi anthu angati anaonjezeredwa ku mpingo?_____
   - Mu ndime 42 ndi zinthu zinai ziti zimene iwo anadzipereka kuzichita?
     _____
     _____
     _____
   - Mu ndime 46 anapita kangati ku kachisi?_____
     _____
   - Mu ndime 47 ndani anali ku onjeza mu mpingo iwo anali kupulumutsidwa?_____
     _____

MPINGO ULI NDI MA UDINDO A PADERA

9. Werengani Machitidwe 1:8
   - Ndi chiani chomwe okhulupilira anafunika kuchitira a mbuye?_____
     _____
   - Anayenera kupita kuti?_____
     _____
   - Mphamvu zochitia umboni zinachokera kuti?_____
     _____

10. Werengani Marko 16:15
   - Kodi ophunzira anayenera kupita kuti?_____
     _____
   - Anayenera kuchita chiani?_____
     _____
   - Anayenera kulalikira kwayani?_____
     _____

11. Werengani Agalatiya 6:1-2
   - Ndi ma udindo awiri oti amene aKhristu ayenera ku kukwaniritsa aKhristu anzao?_____
     _____

12. Werengani Agalatiya 6:10
   - Tiyenera kuchitira anthu zabwino maka maka yani?_____
     _____

MPINGO UKHALIRA MGWIRIZANO INA KHULUPILIRA

13. Werengani Machitidwe 11: 25-26
   - AKhristu ali ndi chilakolako ndi mpata wokumana pamodzi kupembedza ndi ku santhula za mBaibulo. Kodi ndi kuti kumene Paulo ndi Banaba anakumanilani ndi okuluphilira?_____
     _____
   - Anakhala masiku angati pamalopo ndi ku kumana ndi mpingo?
     _____
     _____

14. Werengani Yohane 4:23-24
- Chimodzi cha zifukwa zomwe mpingo una khaziki tsidwaira ndi chiti?

_____

15. Werengani Ahebri 10:25
- Nichiani chimene sitiyenera kulephera kuchita?_____

_____

MAFUNSO AZO KAMBIRANA

1. Mpingo wanu umagwapo bwanji pa so falitsa uthenga wa Khristu kwa ena? Munga thandize bwanji anthu ena mmaiko ena?

2. Ena madalitso a padera amene adza chifukwa cho sonkhana pamodzi ndi otani?

3. Ndi njira zotani zimene mKhristu anga gweepo msonkhano wa mpingo?

Ndichofunika kwambiri kuti inu muzipita kwiri kawiri kumpingo umene uphunzitsa choonadi cha Khristu. Mufunse thandizo kumpingo umene unakupatsani maphunziro awa . Lili lonse muyenera kupita kukachisi kotero kuti mukaphunzire za mulungu ndi kukula ngati Yesu. Mfunsani za Maphunziro akukhala m'modzi wa a mu mpingu kuti inu mugwepo panchito yoyendetsa mpingo.

Lembani ndime yo loweza: Mateyu 16:18

_____
_____
_____
_____
_____
_____